## Kalatayi ikukupatsani uthenga wa mdulidwe wa abambo ndi kuteteza kachirombo ka HIV.

**Kodi mdulidwe wa a bambo ndi chiyani?**

Mau oti “mdulidwe wa abambo”amatanthauza kudula songa la khungu la chokodzera cha a bambo.Pa dziko lonse la pansi,mdulidwe wa abambo umapangidwa mu mipingo,chikhalidwe, zaumoyo ndi pa zifukwa zina.Pafupifupi abambo makumi atatu mwa abambo chikwi chimodzi chili chonse pa dziko lapansi ndi odulidwa.Mau oti” mdulidwe wa kuchipatala wa abambo “amatanthauza kuchotsedwa kw a songa ya chokodzera cha abambo ndi munthu ophunzitsidwa bwino wa chipatala.Pali mitundu ina ya mdulidwe,yotchedwa “mdulidwe wa chikhalidwe”zomwe zimakhudza mitundu yosiyanasiyana ya kadulidwe ka nsonga ,nthawi zambiri zimapangidwa ndi anthu osati achipatala.

**Kodi zodziwika zokhudza mdullidwe wa abambo ndi katetezedwe ka kachirombo HIV ndi ziti?**

Akafukufuku atatu posachedwapa anayesa ngati mdulidwe wa abambo wa kuchipatala ungateteze abambo kutenga kachirombo ka HIV kupyolera mukugonana.Akafukufuku amenewa anali ndi abambo oposa 10,000 ochokera ku Kenya,Uganda ndi South Africa.Akafukufuku anapeza kuti abambo anali ndi theka la mpata oti sangatenge kachirombo ka HIV kulekana ndi abambo omwe sanadulidwe.Izi zikutanthauza kuti,mdulidwe unapezeka kuti ndi othandiza kuteteza abambo kutenga kachirombo ka HIV.Njira ina yofotokozera izi ndi yoganizira abambo khumi omwe akhoza kutenga kachirombo ka HIV kuchokera mukugonana kosadziteteza ndi mai amene ali ndi kachirombo ka HIV.Pakati pa abambo khumi amenewa, mdulidwe ukuyembekezeka kuteteza abambo asanu ku kachirombo ka HIV.

Mdulidwe wa abambo wa kuchipatala ndi njira yothandiza kwa abambo kuti uchepetse mpata otengera kachirombo ka HIV.Komabe,mdulidwe supeleka chitetezo chonse ku kachirombo ka HIV.Chifukwa cha ichi,mdulidwe uzikhala oonjezera ku njira zina zodziwika kuteteza kachirombo ka HIV,kuphatikiza kugwiritsa ntchito makondomu molondola ndi nthawi zonse.

**Kodi zodziwika zina za mdulidwe wa abambo ndi ziti?**

Pali mfundo ina yofunikira yokhudza mdulidwe wa abambo omwe abambo ndi amai ayenera adziwe.Mdulidwe wa abambo suteteza amai kutenga kachirombo ka HIV.Abambo omwe ali ndi kachirombo ka HIV ndipo anadulidwa akhoza kupatsira kachirombo ka HIV kwa abwenzi awo.Ndi zoona kuti abambo ali ndi mpata ochulukirapo kupatsira kachirombo ka HIV kwa bwenzi lawo panthawi yomwe mdulidwe wangochitika kumene,Chilonda chake chisanapole.Chifukwa cha ichi,Bambo yemwe wangodulidwa kumene akuyenera kudikira chilonda chakekuti chipole bwinobwino asanayambe kugonana.



Ngati muli ndi mafunso kapena mukufuna uthenga wochulukirapo, chonde pitani ku kiliniki yakafukufuku, ngati muli ku :

Blantyre, Queen Elizabeth Central Hospital

Ngati muli ndi mafunso kapena nkhawa zofunikira mwansanga, muthanso kuwapeza:

Dr. Makanani pa 01 875 129 ngati muli ku  Blantyre

Version 1.0, 26 January 2012

# Uthenga okhudza mdulidwe wa abambo ndi kuteteza kachirombo ka HIV

